UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO

NTHAMBI YOWONA ZANYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

# NYENGO MSABATAYI


## KUYAMBIRA PA 17 FEBRUARY MPAKA PA 23 FEBRUARY 2025

## NYENGO M'SABATA IKUBWERAYI

**Sabatayi ikuyembekezeka kukhala ya mvula m'madera ochuluka** kamba ka dera lodzetsa mvula la ITCZ. **Chiopsezo cha kusefukira kwa madzi mwadzidzidzi** chikhalanso chokwera m'madera omwe madzi amasefukira kawirikawiri.

## NYENGO MU SABATA YANGOTHAYI

M'madera ambiri kunagwa mvula yochuluka. Ku chigawo cha kumpoto: ku Iponga ku Karonga ndi komwe kunagwa mvula ya mulingo okwera kwambiri wa 103.7 mm pa 13 February 2025 pomwe ku chigawo cha pakati inali ya mulingo wa 33.7 mm tsiku lomwelo koma ku Dedza. Ku chigawo cha kum'mwera, inagwa ku Chikwawa pa Boma ya mulingo wa 84.6 mm pa 15 February 2025.
Mapu ali m'musimu akuonetsa ena mwa madera omwe analandira mvula msabata yangothayi.




*Mapu: akusonyeza kagwedwe ka mvula pa 12, pa 13 komanso pa 15 February, 2025*

## MALANGIZO M'SABATALI

- **Madzi osefukira mwadzidzidzi:** Tikhale tcheru ndipo tipewe kuoloka madzi osefukira kapena othamanga kuti titeteze miyoyo yathu
- **Mvula ya Mabingu:** Kukamagwa mvula ya mabingu tikuyenera kubisala pamalo otetezeka bwino ndipo tipewe kubisala pansi pa mitengo.
- **Chinyezi:** Tikhale osamala ndi **nyumba kapena zimbuzi** zomwe zanyowa kwambiri ndi mvula chifukwa zitha kugwa nthawi ina iliyonse.

***Kuti mudziwe zambiri funsani kwa:***


*The Director, Department of Climate Change and Meteorological Services, Ministry of Natural Resources and Climate Change, P. O. Box 1808, Blantyre, Malawi. Tel: (265) 882 266 579; Email: metdept@metmalawi.gov.mw , Website: www.metmalawi.gov.mw*


**Malo osindikizira: Blantyre** **Yatulutsidwa Lamulungu pa 16 February, 2025**